-Mu phunziro lotsatila, tidzaphunzira zimene zinachitika kwa Abulamu m'dziko la Kanani.



PHUNZIRO LA 19

1. Kodi anthu amene anabadwa pambuyo pa chigumula ndi makolo a ndani?

-Ndi makolo athu.

1. Kodi makolo athu amkadziwa za Mulungu?

-Inde.

3. Kodi makolo athu amkadziwa bwanji za Mulungu?

-Makolo athu amkadziwa za Mulungu chifukwa chakuti anthu akuluakulu amkawawuza anthu ang'onoang'ono za Mulungu ndi chigumula.

4. Kodi anthu akuluakuluwo amkawawuza chiyani za Mulungu ndi chigumula anthu ang'onoang'ono?

-Anthu akuluakuluwo amkawawuza anthu ang'onoang'ono kuti Mulungu amadana ndi tchimo, chomcho Iye anawawononga anthu onse kupatula Nowa ndi banja lake.

5. Kodi makolo athu amkadziwanso bwanji za Mulungu?

-Kachiŵiri, Makolo athu amkadziwa za Mulungu chifukwa chakuti utawaleza umkawawuza za Mulungu.

6. Kodi utawaleza umkawawuza chiyani makolo athu za Mulungu?

-Utawaleza umkawawuza makolo athu kuti Mulungu amaŵakonda anthu onse ndipo sadzaliwononganso dziko la pasi ndi chigumula cha madzi.

7. Kodi makolo athu amkadziwanso bwanji za Mulungu?

-Kachitatu, makolo athu amkadziwa za Mulungu chifukwa chakuti, mlengalenga, mapiri, nyanja ndi mitengo, zimkawawuza iwowo za Mulungu.

8. Kodi mlengalenga, mapiri, nyanja ndi mitengo imka-

wawuza chiyani makoloa athu za Mulungu?
-Zimkawawuza kuti Mulungu yekha ndi Mulungu, ndipo anthu ayenera kumamutsatira Mulungu yekha.

9. Kodi makolo athu ambiri amkakhulupilira za Mulungu?
-Iyayi.
-Anthu ochepa okha ndi amene amkakhulupilira mwa Mulungu.

10. M'malo momutsatira Mulungu, kodi ambiri mwa makolo athu amkamutsatira ndani?
-Amkamutsatira Satana ndi bodza lake.

11. Kodi Satana amkawawuza kuti adzichita chiyani makolo athu?
-Satana amkawawuza makolo athu kuti adzipembedza dzuwa, mwezi ndi nyenyezi.
-Satana amkawawuzanso makolo athu kuti adzipembedza mizimu.
-Satana amkawawuza makolo athu kuti adzipembedza zosema za miyala ndi mitengo zowoneka ngati anthu.

12. Kodi chifukwa chiyani Mulungu samkafuna kuti anthu onse adzikhala pa malo amodzi?
-Mulungu samkafuna kuti anthu onse adzikhala pamodzi chifukwa chakuti samkafuna kuti iwowo amuyiwalire Iye.
-Mulungu samkafuna kuti anthu onse adzikhala pamodzi chifukwa chakuti samkafuna kuti machimo awo achuluke.

13. Kodi chifukwa chiyani anthu anayamba kumanga msanja ku Babulo?
-Chifukwa chakuti anthu anali onyada kwambiri.
-Chifukwa chakuti anthu amkafuna kuti atchuke.

14. Kodi Mulungu samkaŵawona anthuwo pamene iwo anayamba kumanga msanjayayitaliyo?



-Mpulumutsi adzabwera kudzagonjetsa mphamvu ya Satana.
-Mpulumutsi adzamugonjetsa Satana, ndikuŵanjanitsanso anthu ndi Mulungu.

-Mpulumutsi adzamugonjetsa Satana, ndikuŵadalitsa anthu onse pa dziko la pansi.

-Kodi Abulamu amkakhulupilira m'malonjezo a Mulungu?
-Inde.

-Abulamu amkakhulupilira kuti Mulungu sanganame.
-Abulamu amkakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene anganene zowona.

-Tiyeni tiŵerenge zimene Abulamu anachita, Mulungu atapereka malonjezo amenewa:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 12:4-5

4-Abulamu anali wa zaka 75 pamene amkachoka ku Halani monga m'mene AMBUYE adamulamulira, ndipo Loti anapita naye limodzi.
5-Abulamu anatenga mkazi wake Salayi, Loti, mwana wa mng'ono wake, pamodzi ndi chuma chake chonse, ndi atchito ake omwe amene anali nawo ku Halani. Anawuyamba ulendo wopita ku Kanani. Ndipo anafika ku Kanani.

-Mulungu atapereka malonjezo kwa Abulamu, Abulamu anatenga mkazi wake Salayi, mwana wa mng'ono wake, Loti, ndi chuma chake chonse, ndipo anamutsatira Mulungu kumene Iye anaŵatsogolera.

-Kodi Mulungu anamutsogolera Abulamu kupita kuti?
-Mulungu anamutsogolera Abulamu ku malo atsopano kotchedwa Kanani.

-Chifukwa chakuti Hava anali osabereka.

-Ngakhale kuti Abulamu analibe ana, Mulungu anamulonjeza Abulamu kuti adzakhala ndi zidzukulu zambiri.

-Chachiŵiri, Mulungu anamulonjeza Abulamu kuti amudalitsa.

-Tiyeni tiŵerenge chimene Mulungu anamulonjezanso Abulamu:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 12:3

3-[AMBUYE anati], “Ndidzaŵadalitsa onse amene adzakudalitse iwe, ndipo ndidzawatembelera onse amene adzakutembelere iwe. Mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzapeza madalitso kudzera mwa iwe.”

-Chachitatu, Mulungu analonjeza kuti adzaŵadalitsa onse amene adzamudalitse Abulamu, ndipo adzaŵatembelera onse amene adzamutembelera Abulamu.

-Chachinayi, Mulungu analonjeza kuti adzaŵadalitsa anthu onse kupitira mwa chidzukulu chimodzi cha Abulamu.

-Lonjezo lakuti Mulungu adzaŵadalitsa anthu onse kupitira mwa chidzukulu chimodzi cha Abulamu, ndi lonjezo lopambana kwambiri kuposa malonjezo ena onse.

-Kodi chidzukulu cha Abulamu chimenechi ndi ndani, chimene anthu onse adzadalitsika kupitira mwa icho?
-Mpulumutsi.
-Kodi Mpulumutsi adzapanga chiyani?

-Mpulumutsi adzabwera kudzagonjetsa mphamvu ya tchimo.
-Mpulumutsi adzabwera kudzagonjetsa mphamvu ya imfa.



-Inde.

15. Kodi Mulungu amaŵadziwa maganizo a anthu onse?
-Inde
-Munthu asanayambe kuganiza maganizo, Mulungu amakhala ataŵadziŵa kale maganizowo.

16. Kodi Mulungu amaŵadziwa mawu a anthu onse?
-Inde.
-Munthu asanayambe kulankhula mawu, Mulungu amakhala ataŵadziwa kale mawuwo.

17. Mulungu amazidziwa zochita za anthu onse?
-Inde.
-Munthu asanayambe kuchita chinthu china chilichonse, Mulungu amakhala atachidziwa
kale chinthu chimene akufuna kuchichitacho.

18. Kodi Mulungu amayiwala za anthu?
-Iyayi.
-Mulungu sayiwala zimene anthu akuganiza.
-Mulungu sayiwala zimene anthu amanena.
-Mulungu sayiwala zimene anthu amachita.

19. Kodi Mulungu anachita chiyani anthu atayamba kumanga msanja yayitali?
-Mulungu anaŵapatsa anthu zilankhulo zosiyanasiyana kuti anthuwo asamamvane.

20. Kodi china ndi chiyani chimene anachita Mulungu atatha kuŵapatsa anthu zilankhulo zosiyanasiyana?
-Mulungu anaŵabalalitsira anthu ku malo osiyanasiyana a pa dziko lonse la pansi.

21. Kodi makolo athu anafika bwanji kuno?
-Anabwera kuno poyenda ndi miyendo ndi zombo mu zaka

zambiri zapitazo.

-Makolo athu amene anabadwa pambuyo pa Nowa samkamumvera Mulungu, ndipo anamanga chipilala chachitali kwambiri ku Babulo.

-Makolo athuwo anatsata bodza la Satana osakhala zowona za Mulungu.

-Anatsata njira yawo, ndipo anamukana Mulungu.

-Ngakhale kuti Makolo athuwo anamukana Mulungu, kodi Mulungu anazisiya zimene anakhoza zofuna kwapulumutsa anthu?
-Iyayi.

-Ngakhale kuti makolo athuwo anamukana Mulungu, kodi Mulungu anazisiya zimene anakhoza zotumiza Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Mulungu akangopereka lonjezo, nthaŵi zonse amakwanilitsa lonjezolo.

-Mulungu anamupatsa Adamu ndi Hava lonjezo lotumiza Mpulumutsi m'munda mwa Edeni.

-Mulungu sadzaswa lonjezo Lake.
-Mulungu anapereka lonjezo kwa Seti, Enoki ndi Nowa lakuti adzatumiza Mpulumutsi.

-Mulungu sadzaswa lonjezo Lake.

-Ngakhale kuti makolo athu anamukana Mulungu, Mulungu sanazisiye zimene anazikoza zotumiza Mpulumutsi.



-Mulungu anankhula kwa Abulamu ndi mawu ake chifukwa chakuti pa nthaŵi imeneyo Buku la Mulungu linali lisanalembedwe.

-Kodi Mulungu amalankhula bwanji kwa ife masiku ano?

-Masiku ano Mulungu salankhula kwa ife ndi mawu Ake.
-Masiku ano Mulungu amalankhula kwa ife kupitira mu Buku Lake, Bayibulo.

-Tikhoza kumaŵamva Mawu a Mulungu poŵerenga M'buku Lake.

-Tikhoza kumazidziwa zimene Mulungu amatiwuza ife poŵerenga Mawu Ake M'buku Lake, Bayibulo.

-Mulungu atalankhula kwa Abulamu, Iye analonjeza china chake.

-Apa pali zimene analonjeza Mulungu kwa Abulamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 12:2

2-[AMBUYE anati kwa Abulamu] "Ndidzakusandutsa kukhala kholo la mtundu wawukulu, ndipo ndidzakudalitsa ndikukusandutsa wotchuka, kotero kuti udzakhala ngati dalitso kwa anthu ena."

-Choyamba, Mulungu anamulonjeza Abulamu kuti adzakhala ndi zidzukulu zambiri zimene zidzakhale mtundu wawukuru.

-Kodi pa nthaŵi imeneyo, Abulamu ndi Hava anali ndi ana angati?
-Palibe.

-Kodi chifukwa chiyani Abulamu ndi Hava analibe ana?

-Anthu a mu mzinda wa Uli amkamukhulupilira Satana ndi bodza lake.
-Anthu a mu mzinda wa Uli anali oyipa kwambiri.

-Mulungu anamuwonekera Abulamu, akukhala mu mzinda wa Uli.

-Izi ndi zimene ananena Mulungu kwa abulamu:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 12:1

1-Tsiku lina AMBUYE anamuwuza Abulamu kuti, "Choka ku dziko kwako kuno.Uŵasiye abale ako ndi banja la bambo ako, ndipo upite ku dziko limene nditi Ndikusonyeze."

-Kodi Mulungu anamuwuza Abulamu kuti achite chiyani?

-Mulungu anamuwuza Abulamu kuti achoke ku dziko lake, ndipo apite kumene Mulunguyo akamutsogolere iye.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuwuza Abulamu kuti achoke ku Ula ndi dziko lake?

-Chifukwa chakuti anthu a ku Ula samkakhulupilira mwa Mulungu ndi zowona Zake.

-Chifukwa chakuti anthu a ku Ula amkakhulupilira mwa Satana ndi bodza lake.

-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuŵasiyanitsa anthu amene amkamukhulupilira Iye ndi amene samkakhulupilira mwa Iye.

-Kodi Mulungu analankhula bwanji kwa Abulamu?
-Mulungu analankhula kwa Abulamu ndi mawu Ake.



-Ngakhale kuti makolo athu anamukana Mulungu, Mulungu anafunitsitsabe kuti amutumize Mpulumutsi kuti adzaŵapulumutse anthu ku machimo.

-Ngakhale kuti makolo athu anamukana Mulungu, Mulungu anafunitsitsabe kuti amutumize Mpulumutsi kuti adzaŵapulumutse anthu ku imfa.

-Ngakhale kuti makolo athu anamukana Mulungu, Mulungu anafunitsitsabe kuti amutumize Mpulumutsi kuti adzaŵapulumutse anthu kwa Satana.

-Kodi anthu angamuletse Mulungu kuti asatumize Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Kodi anthu angamuletse Mulungu kuti asatumize Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Kodi ziwanda zingamuletse Mulungu kuti asatumize Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Kodi Satana angamuletse Mulungu kuti asatumize Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Kodi ndi ndani amene angamuletse Mulungu kuti asatumize Mpulumutsi?
-Palibe.

-Mulungu akakhoza zotumiza Mpulumutsi, palibe amene angamuletse Iye.

-Chifukwa chakuti makolo athu anakana kumumvera Mulungu, Mulungu anasankha munthu m'modzi kuti atumize Mpulumutsi kupitira mwa iye.

-Dzina la munthu amene Mulungu anamusankha linali Abulamu.

-Mulungu anasankha zotumiza Mpulumutsi kupitira Mwa Abulamu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anasankha Abulamu kuti atumize Mpulumutsi kupitira mwa iye?

-Kodi Mulungu anasankha Abulamu chifukwa chakuti anali osachimwa?
-Iyayi.

-Abulamu anali ochimwa.
-Abulamu anali chidzukulu cha Adamu.
-Abulamu anabadwira mu tchimo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamusankha Abulamu?

-Abulamu amkakhulupilira kuti Mulungu anali oyera.

-Abulamu amkakhulupilira kuti iye anali ochimwa.

-Abulamu amkakhulupilira kuti tchimo lake limkayenera kulandira chilango cha imfa.

-Abulamu amkakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene anali oyenera kumupulumutsa iye.

-Abulamu amkakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi.



-Chifukwa chakuti Abulamu amkakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu anasankha zotumiza Mpulumutsi kupitira mwa Abulamu.

-Bambo ake a Abulamu anali Tera.
-Tera anali chidzukulu cha Shemu.

-Kodi mukuŵakumbukira mayina a zidzukulu za Nowa?
-Shemu , Hamu ndi Yafeti.

-Abulamu anali chidzukulu cha Shemu, m'modzi mwa ana a Nowa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 11:27 ndi 29-30

27-Nazi zidzukulu za Tera: Tera anabereka Abulamu, Nahori ndi Harani. Harani anabereka Loti.
29-Abulamu ndi Nahori anakwatira. Abulamu anakwatira Salayi, ndipo Nahori anakwatira Milika mwana wa Harani, amene analinso bambo ake a Isika.
30-Sarayi analibe mwana chifukwa chakuti anali osabereka.

-Tsiku lina Abulamu anakwatira.
-Abulamu anakwatira mkazi dzina lake Sarayi.

-Abulamu ndi Salayi analibe ana.

-Kodi chifukwa chiyani Abulamu ndi Salayi analibe ana?
-Chifukwa chakuti Sarayi anali osabereka.

-Abulamu ndi Salayi amkakhala mu mzinda wa Uli.

-Anthu a mu mzinda wa Uli samkamukhulupilira Mulungu ndi zowona zake.